

# NDIKOYENELA KUTI AMAYI ONSE AKHALE NDI OWAYANG'ANIRA AMENE IWO ASANKHA OKHA PANTHAWI YA MATENDA, POBEREKA, KOMASO NTHAWI IMENE MWANA WAGOBADWA KUMENE

**Kuthandizidwa maganizo:  
kulimbikitsa mtima pamene  
mzimayi oyembekezera ali  
munthawi yofuna kuchira**



- ✓ Kumulimbikitsa komaso kumusisita pamsana pamene uluru wachuluka kuti uluru uchepe
- ✓ Kuwapukuta amayi oyembekezera thupi lawo lonse ndikamsalu konyowa kuti amve mphepo yabwino
- ✓ Kambiranani ndi mzimayi oyembekezera pazomwe zikuchitika and onetsetsani kuti wamvetsetsa zomwe mzamba wakuchipatala akufotokoza
- ✓ Mulimbikitseni mzimayi amene wabwera kudzachira kukodza maola awiri aliwonse ndiposo kusamba pamene matenda ayamba ngati wasankha kutero
- ✓ Ndibwino mzimayi amene matenda ayamba kukhala ndi munthu omudikilira komaso omuthandizira kuyenda pomwe matenda ayamba
- ✓ Muthandizireni mzimayi kuti akhale opanda mantha komaso kumuphunzitsa kapumidwe kabwino pamene matenda awawa

## Kulankhulana

- ✓ Mumvetsetse malangizo a azamba ndipo wonetsansi kuti mayi oyembekezera wamvetsetsa malangizowo
- ✓ Muthandizireni mzimayi oyembekezera kuti afunse mafunso okhudzana chisamaliro chake ndipo wonetsansi kuti wapeza umphungu onse omwe amayenera kulandira
- ✓ Wonetsansi kuti azamba akumvetsetsa ndi kuperekzo zofunika kwa mzimayi oyembekezera monga ngati mankhwala othandizira uluru



## Chakudya ndi madzi

- ✓ Konzani ndikusunga chakudya ndi madzi pafupi, pamene chakudya chafunikira athandiziren kuwadyetsa komaso kuwamwetsa madzi



## Zoyang'anira

- ✓ **Kutaya magazi:** pamene mzimayi wachira kumene ndibwino kumufunsa pafupipafupi ngati akutaya mangazi komaso kuti ayang'ane malo ogona ngati akutaya magazi Adziwitseni azamba pamene mwaona kuti akutaya maagazi.
- ✓ **Zizindikiro zina zoopsa:** Pamene mzimayi oyembekezera akumva zizindikiro ngati chizumba zumba, kufooka kapena kumva ngati afuna kukomoka adziwitseni azamba



## Chisamaliro cha mwana

- ✓ Onetsetsani kuti thupi lamwana ndi lamayi wake ndilogundana nthawi zonse pamene wabadwa kumene
- ✓ Limbikitsani kuyamwitsa mwana pomwe wabadwa kumene
- ✓ Muwadziwitse pamene mwaona magazi pamchombo pa mwana komaso panthawi yomwe mwaona kuti akuvutika kupuma
- ✓ Athandizireni azamba pachisamaliro chamwana komaso kumveka dzovala
- ✓ Muthandizireni mzimayi kuyamwitsa mwana msanga komaso pafupi pafupi
- ✓ Musamulekenitse mwana kwa mayi wake pokhapokha a chipatala atakuuzani



## Kukhala othandizira

- ✓ Mukuyenera kunkhala pafupi ndi chipinda chochiliramo azimayi oyembekezera ndikuwathandiza anamwino pamene pafunika kutero
- ✓ Akumbutseni azamba nthawi yomwe akuyenela kudzamuunika odwala



## Wonyamula muuni

- ✓ Yatsani muuni wanu pamene amzamba akuwaona amayi oyembekezera komanso panthawi yomwe akuchira

